



## **Mennonite World Conference**

A Community of Anabaptist  
related Churches

## **Congreso Mundial Menonita**

Una Comunidad de  
Iglesias Anabautistas

## **Conférence Mennonite Mondiale**

Une Communauté  
d'Eglises Anabaptistes

### **NGODYA ZA MENNONITE WORLD CONFERENCE (MWC)**

#### **Masomphenya (Vision)**

Mennonite World Conference (MWC) ndi Bungwe lomwe linakhazikitsidwa ndi cholinga choyanjanitsa mipingo yonse ya Anabaptist pa Dziko lonse lapasi ku chiyanjano cha anthu wokhulupilira, kupembedzera, kutumkilana komanso kulalikila Uthenga wabwino.

#### **Zolinga (Mission)**

Bungweli linakhazikitsidwa kuti likhale: (1) Chiyanjano cha anthu okhulupilira padziko lonse la pansi m'chikhulupiro cha Anabaptist, (2) Kulimbikitsa ubale pakati pa mipingo ya Anabaptist pa dziko lonse la pansi, (3) Kukhala m'chiyanjano ndi mipingo ina komanso mabungwe a Chikristu.

#### **Zikhulupiliro za MWC Dziko Lonse Lapansi (MWC Shared Convictions)**

Mwachisomo cha Mulungu, timafunitsitsa kukhala mmoyo uno ndi cholinga chofalitsa Uthenga Wabwino wa chiyanjanitso mwa Yesu Khristu. Monga thupi limodzi mwa Khristu, nthawi zonse komansoponse-ponse tamangililika pa mfundo zotsatirazi kukhala ngodya za chikhulupiliro chathu:

1. Mulungu amadziwika kwa ife monga Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera, Mlengi amene amafuna kubwezeretsa mtundu wa anthu wotaika pakuwayitana kuti akhale okhulupilika m'chiyanjano, kulambira, kutumikirana wina ndi mnzake ndi kuchitira umboni za Yesu.
2. Timazindikila Yesu kukhala mwana wa Mulungu; kudzera mwa Moyo wake ndi ziphunzitso zake, masautso omutengela ku imfa yake ndi kuukanso kwa akufa mwa izi zonse lye anationetsera ife mmene tingakhalire ophunzira okhulupilika pamene anawombola dziko lapansi ndi kupeleka moyo wosatha.
3. Monga Mpingo, ndife gulu la anthu okhulupilira Mulungu amene mwa Mzimu wake atiyitanila ife kuchokela kuuchimo, natizindikilitsa Yesu Khristu kukhala Ambuye ndikulandila ubatizo mwakubvomeleza mwa chikhulupiliro ndi kutsata Yesu mmoyo uno.
4. Monga anthu achikhulupiliro mwa Mulungu, timabvomereza Baibulo monga maziko achikhulupiliro chathu komanso moyo wathu ndikulimasulira pamodzi pansi pa chitsogozo kapena ulamuliro wa Mzimu Woyera, mowunikiridwa kwa ife mwa Yesu Khristu kuti tizindikire chifuniro cha Mulungu mwakumvera kwathu.
5. Mzimu wa Yesu Khristu amatilimbikitsa kukhulupiiira Mulungu mmadela onse a moyo uno kukhala anthu odzetsa mtendere pokana makangano kukonda adani athu, kutsata chilungamo, ndikugawana nawo chuma amene ali osowa.
6. Timakhulupiiira kusunkhana pamodzi kawiri-kawiri kulambira Mulungu, kukondwelera mkunyema mkate wa Ambuye ndi kumva Mau a Mulungu ndi mtima wosweka.
7. Monga chiyanjano cha anthu osiyanasiyana koma a chikhulupiliro chimodzi komanso moyo tilibe malire potengela kumene munthu amachokela, mtundu wa munthu, kupeza kapena kusowa kwa munthu, mwamuna kapena mkazi kapena chiyankhulo. Timafunitsitsa kukhala mdziko posatsatira mphamvu za oipayo. Koma kulalikila Uthenga wa Chisomo cha Mulungu mwa kutumukila ena, kusamala chilengedwe, ndi kulalikila ena za Yesu Khristu Ambuye Wathu.